

Zochita zamaphunziro akunyumba

KUPUNZIRA
kumachitika
kulikonse, nthawi
iliyonse nakuli
aliyense



EENET – Enabling Education Network
PO Box 422
Hyde
Cheshire
SK14 9DT
UK

 www.eenet.org.uk

 info@eenet.org.uk

 +44 (0)7929 326 564



This work is licensed under the Creative Commons Attribution-NonCommercial-ShareAlike 4.0 International License. To view a copy of this license, visit <http://creativecommons.org/licenses/by-nc-sa/4.0/>

Tsamba la zamkati

Chiyambi		4	
Kusintha machitidwe a nchito za ana ali ndi zosautsa pophunzira ndiponso ali ndi chilema pathupi pao		6	
Mndandanda wazochita		8-73	
Buku la ABC	8	Pangani mapikicha amalo okhalamo akwanu	40
Kupanga nsanja	10	Pangani kadoli wasokosi	42
Kupanga mndandanda wa zosautsa	11	Nsolo kapena sewero lazowerenga lolinga nalo	44
Zamanambala	13	Kuyang'anira zachilengedwe	46
Kuphika ndi manambala	16	Nyimbo yatsopano, maimbidwe akale	49
Pagani sewero laphabwa	18	Nthano yosokonezeka	50
Kodi muona zomwe ndiona?	20	Bzalani mbewu ndipo muionelere ikule	53
Lembani chithunzi thunzi chanyama	21	Kuwerenga pamodzi	55
Lembani chithunzi-thunzi chamzinda wanu woganizira	23	Kufuna-funa zakufa kale	58
Zapamtima	25	Nambala yobisika yachisinsi	60
Yenjamitsani bwato wanu	27	Maonekedwe ndi mapangidwe azinthu muchilengedwe	62
Kupita kumsika	28	Nkhani yozungulira	64
Mau angati ...?	30	Thokozani ngwazi yakwanu	66
Ndikadakhala mtsogoliri wadziko	31	Kufuna-funa chokoma	67
Kuyankhulana ndi munthu wachikulire	33	Mafunso makumi awiri	69
Pangani chitsulu (chida kapena makina)	35	Kalata kwa aphunzitsi	71
Chionetsero chazakutha	37		
Kupanga mdandanda wazinthu	39		

Chiyambi

Kodi zochita izi ndizayani?

- Zochita izi ndi **zamabanja onse** a ana ali ndi zosausa pamatupi pao ngakhale amene alibe.
- Zochita izi ndi za **aliyense** - amai ndi atate, osunga ana, atsikana ndi anyamata, anthu achichepele, obadwa nao pamodzi (abale ndi alongo), ambuye akazi ndi abuye amuna, amalume ndi atate akazi. Kuli mpata waukulu wakuphunzira pamodzi.

Kodi ndi zochita zotani zimenezi?

Ili ndi **thumba lazochita zosiyana-siayna** za anyamata ndi atsikana amisinkhu yonse ndiponso makolo ao, owasunga ndi abanja kuti akachite kunyumba. Aliyense akhoza kugwiritsa nchito nfundo zamaganizo ake ndi lingo kuonjezera pazinchito zimenezi.

Ndichifukwa chiyani zochita zimenezi zinapangidwa?

Zochita zimenezi zithandizira njira zambiri .zimene ana aphunziriramo kunyumba. Mungazikumbukire zochita zina chifukwa ana anu amazichita. Zochita zimenezi zithandizira mabanja kuti adziwe **momwe maphunziro achitikira kunyumba** ndiponso momwe maphunziro akunyumba angathandizire kuphunzira kusukulu.

Mogwiritsira nchito zochita zimenezi

Onani pazochita ndi mwana wanu. Muloleni mwana wanu asankhe zochita zomwe zimsangalatsa. Kulibe mndandanda wofunika kulondola pochita zochita zimenezi.

Kuli uthenga oyikika panchito lili yonse, monga zalembedwa munsimu:

Zofunikira: Kabokosi aka kaonetsa chikonzekero chofunikira ndi zinthu zimene mudzafuna kuti muchite nchito. Zochita zina sizifuna zili zonse, zina zifuna phensulo ndi pepala, kapena zinthu zinatha kale nchito, kapena zonyamuliramo katundu kumasitolo ndi zina zomwe zingapezeke pamalo pamene mukhala ndipo sizigulidwa ndi ndalamu.

Zochita: zounikira izi zinalembedwa kuti ana alondole. Ana amene akwanitsa kuwerenga angalondole ndondomeko okha. Ana ena angafunike thandizo lapadera kuchoka kwa abale ao akulu kapena achikulure amene akwanitsa kuwerenga.

Kuonjeza zochita: Nthawi zina nchito zina zinaonjezedwa kupatsa ana okulirapo msinkhu kapena ana ochita bwino nchito yokulirapo mphanvu.

Munsi mwanchito ili yonse muliuthenga wokuthandizirani kusankha zochita zoyenera zamwana wanu, izi ndizo:

Msinkhu: Apa anene za msinkhu wa ana oyenera nchito yoyikika, koma nthawi zambiri ana amisinkhu yonse angachite zochita zolingana. Zotulukamo akatsiriza nchito zingasiyane, mwachitsanzo ana akulu msinkhu angalembe malembo ndi zithunzi-thunzi zooneka bwino.

Kugwapo kwa akulu/abale: Apa anena zakukula kwake kwa mphamvu yothandiza ngati kufunika kuthandiza mwana. Abale ndi alongo akulu akulu angamthandize mwana mwapang'ono kapena kwambiri kapena mwana angachite nchito paiyekha opanda thandizo. Uthenga uyu udzakuthandizani kudziwa ngati mufunika kuti muli pafupi kuchita zanu pamene mwana akuchita nchito yake. Nthawi zina inu kapena abale akulu afunika kupeleka thandizo lalikulu kwa ana ali ndi zosautsa pophunzira kapena uchilema patupi pao.

Zomwe mudzaphunzira ndi zomwe mudzachita: Nchito ili yonse ithandiza mwana kuonjezera nzeru zake, kapena kudziwa kuchita chinthu chatsopano. Kabokosi munsi mwa nchito ili yonse kaonetsa zomwe mwana adzaphunzira munchitoyo. Muzochita zambiri muli kupanga, kumanga kapena kuchita chinthu chomwe chidzathandiza mwana kugwiritsa nchito luso lake. Mwaizo ndi kulumikuzana ndi ena, kugwirizanan (kusewenza), kuchita mwaluso, kuthetsa bvuto, kuganiza mozama ndi kugwirizana kwa thupi. Masukulu ndi aphunzitsi adziwa kuti zaluso izi ndizofunikira. Nthawi zambiri ana sakhalala ndi nthawi yophunzira, kukhazikitsa ndi kukhwimitsa zaluso zimenezi kusukulu. Kunyumba kuli mpata wambiri wophunzira kupyolera mumasewera ndiponso kuchita nchito zatsiku ndi tsiku monga kuphika.

Njira zina zochitiramo nchito: Nchito zambiri muli zoganiza zanjira zina zochitiramo nchito kapena kusintha zochita zamwana ali ndi zosautsa pophunzira kapena ali ndi chilema pathupi pake. Zochita zonse zingachitidwe ndi mwana aliyense koma ena angafunike thandizo pang'ono kapena angafune kugwiritsa nchito njira zina pochita nchitoyo (monga kulemba zithunzi-thunzi kapena kukamba m'malo molemba; kapena kupeputsa zochita). Tsamba yotsatira idzapezeka nfundo zamaganizo zambiri mochitira zinthu munjira zina. Muwadziwa bwino ana anu motero kuti mugadziwe momwe zingawathandizirne nao.

Kumbukirani, kuphunzira kuchitikira pali ponse, nthawi ili yonse.

Kusintha machitidwe a nchito za ana ali ndi zosautsa pophunzira ndiponso ali ndi chilema pathupi pao

Munsi mwa nchito ili yonse mwalembedwa zothandizira momwe tingasinthire nchito za ana ali ndi zosautsa pophunzira ndiponso ali ndi chilema pathupi pao. Mwana ali yense muli momwe aliri kusiyana ndi ena onse motero kuti zothandizira zimenezi zifikira kwa aliyense. Nthawi ndi nthawi ana adzatithandizira kuti tidziwe zomwe akusoweka. Pamene tizolowerana nawo ana tizadziwano bwino kuwalimbitsa ndiponso zomwe angachite bwino kwambiri, zomwe akonda kuchita ndiponso kumene afunika thandizo.

Ndichofunika kuwathandiza ana koma muonetsetse kuti simuwachitira nchito yawo – afunika kuti adzinvere kuti akwanitsa kuchita mawaiwo okha. Osaganiza kuti mwana sangathe kuchita nchito. Mungapeze njira zina zosinthiramo nchito kuti aliyense akwanitse kuichita.

Munsimu mwalembedwa zina zoganiza zothandizira ana ali ndi uchilema opatulika kapena zosautsa pophunzira zopatulika. Zoganiza zimenezi zingasewenzetsedwe panchito ili yonse.

Ara ali ndi zobvuta popenya

- **Gwiritsani nchito malembo akuli akulu:** Ngati kulemba kufunika munchitoyo, onani ngani mwana achipeza chapafupi kuwerenga malembo akulu akulu (makapito) kapena ang'ono ang'ono. Nthawi zina malembo an'ono-ang'ono asewenza bwino chifukwa aonekera kwambiri maonekedwe ake koteru kuti ndi chapafupi kuwerenga ndiponso kuwazindikira
- **Gwiritsani nchito zamitundu ina:** Ngati ndikotheka, gwiritsani nchito mtundu wina kulemba mau akulu-akulu oktsimikiza nfungo mchiganizo, (mwachitsanzo, mau monga 'a' ndiponso 'chi' ndiponso/kapena mau ochita monga 'kanba' ndi 'patsa'). Izi zingapeputse nchito yamwana powerenga kapena kulemba.
- **Gwiritsani nchito zinthu zogwirika ndi manja** popanga kapena kumanga zinthu, motero kuti ana ali ndi zosautsa popenya akhoza kupapasa ndi kugwira-gwira zinthu zomwe akupanga. (mwachitsanzo, pangani nsanja kugwiritsa nchito zinthu zisiyana siyana)
- Kumbukirani kuti ziganizo zanfundo izi zikhoza kuthandiza ana onse, osati amene ali ndi zosautsa popenya okha.

Ara ali ndi zosautsa pakunva:

- **Gwiritsani nchito chilankhulo chathupi ndi manja** ngati inuyo ndi mwana wanu muchidziwa. Mwinanso mukhoza kuphunzira za chilankhulo chathupi ndi manja zofunikira kwambiri pamodzi ndi mwana wanu.

- **Mukhale choyang' anana ndimwana** amene sakunva bwino-bwino ndipo mulankhule mooneka bwino (osakuwa). Mugwirits e nchito **chilankhulo chathupi, kuonetsa pamaso ndiponso kusewenzetsa manja** kuti zithandizire kufotokoza zomwe mutanthauza.
- Muyesetse kuchitira nchito yanu mumalo momwe muli kuwala bwino-bwino kuti mwana aziona ndi kuwerenga milomo yanu. Yankhulani mofasa ndipo osaluma luma mau.
- Pochita nchito sewenzetsani phensulo ndi pepala (kapena choko ndi bolodi) kulemba zomwe mukuchita, komanso mungalembe zithunzi-thunzi kuthandizira kufotokoza zinthu zina.
- Kumbukirani kuti aya maganizo ena angathandizenso ana onse, osati aja okha ali ndi zosautsa pakunva

Ana ali ndi zosautsa poyenda

- **Sungani zones zogwiritsa nchito pafupi:** Muonetsetse kuti zinthu zomwe zifunikira pagwira nchito ziri pafupi pakuti mwana angafikirepo.
- **Muyesetse kugwiritsa nchito zinthu zomwe zithandiza ana mumagwiridwe sizisautsa.** (Mwachitsanzo maphensulo ndi mabopeni akulu-akulu angagwirike mopanda bvuto.)
- **Wathandizireni muzinchito zina** pamene muona kuti ndichofunikira, (mwachitsanzo, mungawathandiza kuponya kadaisi pochita masewera achizungu apabolodi).
- **Malo oseweleramo asakule kwambiri:** Mungasintheko nchito motero kuti zingachitikire mumalo ochepta, amene safuna kuyenda-yenda kwambiri, (mwachitsanzo, masewera yakambisale ndi kufuna funa chuma angachitikire muchipinda chimodzi m'malo mwa nyumba yonse kapena ndi panja).

Ana amene atenga nthawi yayital kuphunzira

- **Muipange yopepuka nchito** ndipo mungachitako gawo limodzi. (mwachitsanzo, mungoimbako ndime imodzi 'yanyimbo yatsopano, maimbidwe akale', osati atatu: lembani mdandanda waufupi ngati ndi 'nchito yolemba mndandanda'). Mwana wanu akhozanso kulemba liu limodzi limodzi m'malo molemba chiganizo chonse kuti aonetse momwe maganizo ake alili.
- **Lembani zithunzi thunzi osati kulemba mau.** Nchito zambiri zigwiritsa nchito kulemba zithunzi-thunzi. Mwanchito zomwe zifuna kuti ana alembe, akhoza kuonetsa maganizo ao mwakulemba zithunzi-thunzi mmalo mwa mau.
- **Zounikira Muzigawe gawe** kuti zikhale ndondomeko zopepuka ndipo mumuuze mwana azichita chinthu chimodzi panthawi imodzi. (Mwachitsanzo, 1) choyamba tengwa phensulo ndi pepala, 2) ndipo lemba kachithunzi-thunzi kopanda mtundu mkati mwake, 3) ndipo ikamo mtundu mkati, 4) potsiriza ukapatse dzina kachithunzi thunzi.)
- **Bwerezani zounikira** kawiri kapena katatu kuti mwana amvetsetse uthenga wake.


Nthawi zonse muwalole ana akutsogolereni. Adzakudziwitsani ngati akunvetsetsa, ndiponso ngati afuna kuchita nchitoyo kapena ai. Wathandizireni moyeyeka koma osawakakamiza. Ichi chithandiza kubvomera kuti nchito ndiyobvuta ndipo mungaisinthe kuti achitire pamodzi. Mukhoza kunena kuti "Ichi chioneka monga chabvutako pang'ono ati? Sitingayese kuchitira pamodzi kodi?"

Buku la ABC

Zofunikira: Maphensulo (ndi yamitundu ngati muli nayo), pepala, ulimbo kapena nsingano kotoni osokera

Zochita:

- Tengani mapepala ndi maphensulo zikhale pafupi.
- Petekani mapepala kuti mupange buku la malembo apopangira mau. Kodi mungafune mapepala angati?
- Pangirani momwe mungalembere malembo monga zithunzi-thunzi. Limodzi tsamba lili lonse? Awiri? Pamodzi ndi zithunzi-thunzi za zinthu/nyama zimene maina ao ayamba ndi lembo limenelo?
- Pangirani ndi kulemba chithunzi-thunzi cha buku. Kumbukirani kuikapo dzina lanu ngati 'wolemba' (analemba buku)
- Ganizirani zamomwe zithunzi-thunzi za malembo zingalembekile. Kodi malembo adzaoneka ngati tumitengo twa anthu kapena ngati tunthambo?
- Patsamba lili lonse muonjezere ndi mau amene ayamba ndi lembo lamu afabeti.
- Petekani bukulo ndipo mupemphe munthu wachikulire alisoke pamsana kugwiritsa nchito nsingano ndi kotoni kapena amate ndi ulimbo.



Kuonjeza zochita:

- Werengani mokweza , kapena mupemphe munthu wina awerenge nkhani ili munsimu

Musokonezo mudziko la afabeti

Tsiku lina amphundu 'e' ndi 'e' anafuna kuti akadzisangalatse. Motero anapita pakati pa mau alionse amene aganizira. Anasinha 'ship' kukhala 'sheep' ndipo sheep anabvumbwa kwambiri ndipo anasokoneze ka. Anasinha 'chick' kukhala 'cheek' ndipo make watunkhuku anafuna funa ana ake tsiku ionse. Anasinha 'stir' kukhala 'steer' ndipi wophika sanadziwe zomwe anali kuchita. Anasinha Will kukhala wheel ndipo anavunvulika mpaka munsi mwa kaphiri. Amphundu anali kungo seka. Koma malembo ena sanazione zokondweretsa zimenezi. 'Potsiriza mkulu wamalembo anati, 'Basi kwatha' ndipo anawatenga amphundi ndikuwaika pakati pa 'slip' ndikuwapereka ku 'sleep'.

- Kodi mungapange nkhani yanu yamalembo mdziko la afabeti?

Msinkhu: Achiambi

Kugwapo kwa akulu/abale: Pakati-kati

Zomwe mudzaphunzira: Afabeti, kukhasikikaka kwachilankhulidwe, malankhulidwe, malembedwe amaina.

Zomwe mudzachita: Luntha, kulunikizana ndi ena, luso lazopanga panga

Njira zina zochitiramo nchito:

- Pangani nyimbo yazamalembo opangira maina.
- Mupemphe munthu wina akuthandizeni kupanga buku.
- Gwiritsani nchito tuminyala tung'ono-tung'ono kapena tumapendelo kupanga afabeti pathebulo kapena pansi.

Kupanga nsanja

Zofunikira: Zonyamuliramo zinthu zolimba kapena pulastiki yolimba, tumabokosi tung'ono-tung'ono, minyala yopamanthala

Zochita:

- Tolani ndi kuika pamodzi zinthu zambiri zili ndi pokhalila pokhazikika. Izi zingakhale mabokosi akale, zoikamo katundu kusitolo zili ndi zotsekela pamwamba, mabuku, tuminyala tung'ono-tung'ono topamanthala, makapu yakulu yakulu ali ndi zapamwamba zake
- Yesani kupanga nsanja ndi zinthuzo. Muona kuti ndi chinthu chotani chomwe mungaike pamwamba pachinzake? Kodi zinthu zazikulu kwambili zili kuti? Kodi mukaika chinthu chaching'ono pansi pansanja yanu, chikuchitika ndi chiyani?
- Kodi nsanja yanu ingakhale yotalimpha motani? Chomwe chipangitsa kuti nsanja yanu iyimilire kapena igwe ndi chiyani? Kodi mungailimbitse bwanji nsanja yanu?



Msinkhu: Achiambi

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Kukhazikika kwazinthu, luso la zopangapanga

Zomwe mudzachita: Kuyesa-yesa, luntha, kulumikizana ndi kudziwa momwe zinthu zikhaliira

Njira zina zochitiramo nchito:

- Uzani munthu wina kuti akuthandizeni kumanga nsanja yanu.
- Ngati mubvutika kuona mugwiritse nchito zinthu zogwirika kuti mungaipapase nsanja.

Kupanga mndandanda wa zosautsa

Zofunikira: Katundu wamapulanga, zinthu zikulu zikulu monga mabokosi yopangidwa ndi pulanga, matheyala yakale etc.

Zochita:

- Mndandanda wazosautsa ndi masewera azochita-chita momwe mumapeseka zinthu zobvuta kuitapo chakuti ufunika kukwerapo kapena kupita munsi mwake mwinanso kujumpha.
- Pezani malo (mkati kapena kubwalo) kwamene mungapangire mdandanda wazosausa. Pezani zinthu zofunikira popanga mdandanda wanu wa zosautsa: mwachitsanzo, tumitengo twamapulanga, minyala ikulu ikulu yopangira moponda, matayera yakale, ziduswa zakatundu wamnyumba.
- Pangirani ndi kumanga mndandanda wanu wazosautsa. Ganizirani za amene adzasewenzetsa mndandanda wazosautsa? Muzipange zikhale zolimba koma osati zokanikiratu.



- Muuyese mndandanda wanu wazosautsa – kodi chilipo chomwe mufuna kusintha? Mupemphe munthu wina akusungireni nthawi pamene mupita mumndandanda wazosautsa. Kodi mungazichite izi mofulumira Kotani?



Msinkhu: Achiambi

Kugwapo kwa akulu/abale: Pakati kati

Zomwe mudzaphunzira: Kupangira, kumanga

Zomwe mudzachita: Kuchita mwaluso, kuthetsa bvuto, kulumikidzana ndi ena, zakakhalidwe kazinthu


Njira zina zochitiramo nchito: Ufewetsenkoni mndandanda wanu wazosautsa kuti muthandizire amene sakukwanitsa bwino-bwino kupidamo kapena amene abvutikira kupenya. Muikemo mayendedwe monga kuvunvulika, kukwawa ndipo/kapena zinthu zongirika ndi manjakuti apapasire njira yawo.

Zamanambala

Zofunikira: Phensulo/bopeni ndi mapepala, choko


Zochita:

- Mukhoza kukulemba chithunzi thunzi chanu papepala, kapena mukhoza kupeza malo yakulu pamene mungalembe chithunzi-thunzi pansi kugwiritsa nchito choko.




- Ili sewero ndi losewera ndi manambala. Kuchokera pamena alemba kuti 'start' mudzayenda mutumizera mpaka mukafike polemba 'finish'. Mukhoza kuyenda mukamzera kowongoka kapena kokhota-khota kapena njira ina ili yonse. (kopitira)
- Pamene mukuyenda mutumizera muonkhese kuika pamodzi manambala ali pamene mupita koteru kuti mudzakhala ndi nambala yothera pamene mwafika pa FINISH.


- Mwachitsanzo: Kodi mungayende munjira zingati zosiyana siyana kuti mupange nambala 8?



1.
 $2 \times 4 = 8$



2.
 $2 + 2 + 4 = 8$



3.
 $3 \times 4 - 4 = 8$
 $(12) - 4 = 8$

Yankho: Pafunika
kupezeka njira
zitatu

- Malamulo ndi awa:

- ⊖ Njira iliyonse ikhale yosiyana ndi zinzake
- ⊖ Kulibe njira idzapita pamalo pena pali ponse kupitilira kamodzi
- ⊖ Pamene mupita panambala iliyonse muikire, muchotsere ndiposo/
kapena kuchulukitsa kuti nambalayo ionjezedwe pamodzi ndi sinzaka.

- Kodi mungapeze njira zotipereka kunambala ya 10? Nanga njira ziwri zotipereka kunambala ya 16? Lembani momwe munali kuonkhesera.
- Ndinjira zotani zina ndiponso manambala akothera ena amene mungapange? Ndinambala yotani yayikulu kwambiri imene mungapange? Ndinambala yotani yaying'ono kwambiri imene mungapane? Mukhoza kupanga manambala angati othera pamodzi?

Kuonjeza zochita:

- Mumpatse mnzanu nambala yothera ndipo mumuuze kuti apeze njira zake. Nkutheka kuti angapeze njira yimene inu mukalibe kuiganizirako!
- Pachithunzi-thunzi chanu muikepo manambala yanu yena. Mungasewenzetse numbalu iliyonse koma chingathandize kwambiri ngati mungagwiritse nchito manambala yang'ono-yang'ono yosapitilira pa 100.
- Mukhozanso kugwiritsa nchito manambala ali ndi mapoint kuti zochita zikuleko. Mwachitsanzo, $0.5 \times 4 = 2$ kapena $2.5 \times 5 = 12.5$.

Msinkhu: Aliyense

Kugwapo kwa akulu/abale: Pakati-kati

Zomwe mudzaphunzira: Kuonkhesa manambala, kuikira, kuchotsera ndi kuchulukitsa

Zomwe mudzachita: Kuthetsa bvuto, kuganiza mozama, kugwirizana ndi ena, kulumikizana ndi ena

Njira zina zochitiramo nchito: Lembani mizera yanchito yanu pansi mwaluso ndi choko. Mulondole njira ndipo zizakuthandizani kukumbukira mowonkhesera manambala moyenera. Musewenzetse manambala 1-5 muchithunzi-thunzi chanu chapansi.

Kuphika ndi manambala

Zofunikira: Phensulo kapena bopeni ndi pepala, Zofunikira pophika, zophikiramo

Zochita:

- Ganizirani chomwe mungafune kuphika. Lembani ndondomeko yamaphikidwe ndi munthu wankulu kapena m'bale wamkulu ngati mufuna thandizo.
- Lembani zonse zofunikira pophika (zomwe muphikira) zomwe mungafune.
- Ganizirani numbala ya anthu womwe mukuphikira. Chili chonse chofunikira pophika chidzafunika mochuluka bwanji kulingana ndi nambala iyi ya anthu? Lembani mtengo wachofunikira chilichonse pambali pake.
- Kodi zinakakhala zochuluka motani kuti munali kuphikira anthu ambiri kachiwiri? Anthu ambiri kudula pakati? Kuonjezerapo anthu awiri?
- Tengani zophikira ndi zophikiramo (miphika yonoka kapena yapamwamba) mudwikonzekere. Pimani zophikira.
- Fotokozerani ndondomeko/zounikira mophikira chophika chanu ndipo ndondomeko iliyonse muilembe. Gwiritsani nchito mau kufotokozerana zamaphikidwe monga 'kudula', 'kubvundula' ndi 'kusakaniza'.
- Londolani ndondomeko iliyonse yamaphikidwe ndipo mungasinthe zounikira pamene mupitiriza, muyesetse kulemba zooneka bwino kuti wina aliyense angalondole maphikidwe anu.
- Mukatsiriza kuphika muitane banja lanu kuti adye zomwe mwaphika.
- Ganizirani momwe mungagawanitsile zomwe mwaphika molingana pakati manambala yaanthu omwe alipo. Munthu aliyense angatenge zipande zingati kapena nunsu zingati? Kodi chilipo chochuluka chakudya kuti anthu angatenge kachiwiri?

Kuonjeza zochita:

- Lembani zamaphikidwe anu mwaluso kuti wina aliyense angalondole zounikira. Auzeni kuti aphike ndipo anene zotulukamo (akuuzeni) kuongoka kwake kwa zounikira ndipo ngati kungafunike kusintha chilichonse.



- Sankhani chophika chomwe mungathe kudula dula zotulukamo zake kupanga magawo-magawo, monga keke, bisiketi kapena kudula zipatso kupanga chakudya chazipatso. Pangani magawo osiyana-siyana ndipo muwalembe (monga chithunzithunzi chili pamwambapo).
- Pangani buku la 'zamaphikidwe' yazophika zanu zones zomwe mukonda

Msinkhu: Aliyense

Kugwapo kwa akulu/abale: Pakati-kati / kwambiri

Zomwe mudzaphunzira: Kuonkhesa manambala, kugwiritsa nchito zamanambala, kupima, kuganizira zophika, kukhazikika kwachilankhulidwe

Zomwe mudzachita: Kuchita zinthu mwaluso, kulumikizana ndi ena, kuthetsa bvuto, kuganiza mozama, kugwirizana

Njira zina zochitiramo nchito:


- Uzani munthu wina akuthandizeni zamaphikidwe.
- Pelekani zounikira mwapakamwa osati kuzilemba.
- Uzani wina wache kuti alembe zounikira.
- Lembani zithunzi-thunzi zandondomeko iliyonse yamaphikidwe

Pagani sewero lapathabwa

Zofunikira: Maphensulo amitundu kapena bopeni, pepala lalikulu, tunthu tung'ono-tung'ono, sizala, kadaisi kapena kadaisi kopangila kunyumba ka pepala

Zochita:

- Tengani mapepala ndi maphensulo zikhale pafupi, ngati ndi kotheka muikepo maphensulo amiyundu-mitundu. Ikani pepala lalikulu limodzi pathebulo kapena pansi.
- Mulembe tumabokosi tokumanizana papepala kuti tupangu kanjira kodutsa papepala, (onani chithunzi-thunzi munsi). Muonetse bwino bwino koyambira ndi kotsirizira.



- Mabokosi ambiri muwasiye opanda chilichonse. Mumalo mwina mulembemo 'tenga khadi'. Ikani malo ena amene adzalongoza osewera kuti apite kutsogolo kapena kumbuyo, mwachitsanzo 'bwelera kumbuyo kawiri', 'osaokeka' Mufunika kalimbeko pang'ono kuti zinthu sikhale zokondweretsa, koma zisalimbe kwambiri kuti chikhale chobvuta kupambana sewero.

- Mudule tumabokosi twina twapepala. Kumbali imodzi yapepala lililonse mwadula mulembeko zounikira/zochita. Mulembe mwaluso kuti mukhale ndi zounikira zosiyana-siyana! Mwachitsanzo:
 - ⦿ Zochita zamasamu: Werengani muma 3, muma 6, muma 8 ...
 - ⦿ Zochita zathupi: Zungulirani katatu, menyani mbama kumutu pang'ono ndipo papasani pamimba pamene mukuwerenga manambala mpaka pa 20,
 - ⦿ Pangani mndandanda wa mau amene amveka molinga
 - ⦿ Imbani nyimbo
 - ⦿ Chulani mizinda ikulu ikulu 5 yamaiko
- Ndi anzaru ena amena musewera nao pangni malamula ya sewero, adzayambira ndani? Chidzachitika ndi chiyani ngati wina walephera kuchita zochita? Ungapemphe thandizo? Ungafune kuti chikupitilire? Mukagwirizana malamulo muyambe kusewera.
- Tumakhadi twazochita mutuike moyangana pansi pafupi ndi sewero lanu. Aliyense atengeteko mbali molondolana kuponya daisi.
- Ngati wina wafikira ponena kuti 'tenga khadi', atengete khadi yanchito. Achite zomwe zalembedwa pakhadi. Ngati wina sakwanitsa onani pamalamulo anu.
- Adzayambilira kufika kothera wapambana.

Msinkhu: Zaka 8 zakubadwa ndi kupitilirapo

Kugwapo kwa akulu/abale: Pakati kati

Zomwe mudzaphunzira: Kukhazikika kwachilankhulidwe: kugwiritsa nchito manabala, zophunzira muumunthu

Zomwe mudzachita: Kulumikizana ndi ena, kugwirizana ndi ena, kuganiza mozana, kuchita zinthu mwaluso

Kodi muona zomwe ndiona?

Zofunikira: Phensulo kapena bopeni ndi pepala

Zochita:

- Lembani chithunzi-thunzi.
- Chotsatira, lembani ndondomeko zamalembewe achithunzi-thunzi.
- Pemphani wina alondole ndondomeko zanu mopanda kuona chithinzi thunzi chanu.
- Akatsiriza, linganizani zithunzi-thunzi. Muganiza bwanji? Ndizolingana kapena zosiyana? Ndichifukwa chiyani zisiyana? Ndichiyani chinakazipangitsa kuti zilinganeko?



Msinkhu: Aliyense

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Kukhazikika kwachilankulidwe; kulemba zounikira


Zomwe mudzachita: Kuchita zinthu mwaluso, chigwirizano, kulumikizana

Lembani chithunzi thunzi chanyama

Zofunikira: Maphensulo ndi mapepala

Zochita:

- Tengani mapepala ndi maphensulo makamama amitundu yosiyana-siyana zikhale pafupi.
- Ganizirani kuti chona anali ndi chitamba monga chanjobvu? Kapena galu anali ndi khungwa pamsana? Kodi izi zinakaoneka bwanji?
- Lembani chithunzi-thunzi chanyama yomwe mukonda yowoneka bwino ili ndi ziwalo zanyama zina.
Zipatseni maina ake ziwalo zanyama zina.
- Ipatseni dzina nyama yanu yokometsetsa. Dzina likhoza kuloza kunyama zina zomwe mwagwiritsa nchito ziwalo zao popanga chithunzi-thunzi chanu.



Kuonjeza zochita:

- **Ganizirani:** Chikhala kuti (mudziko lathu kapena dziko lina? Ndichotani?), chikudya chiyani, Chinveka ngati chiyani polira, chiyenda bwanji? Chinatenga bwanji ziwalo zanyama zina?
- **Kambani/lembani nkhanzi** yachinyamacho.
- **Welengani nkhanzi yotsatira** (kapena mufunse wina akuwelengereni) idzakupatsani nzeru.

Fisi ndi kalulu

Fisi anali kugulitsa ndiwo zamasamba kumsika ndipo nthawi zonse kalulu anali kumnyodola. Sungathamange kupitilra ine, kodi ungakwanitse? Anatero kalulu. 'Ndiwe okalamba ndipo sungathe kuona bwino' .

Anabvina-bvina mozungulira fisi amena anafuna kuti amgwira koma analephera. Kalulu anathawa ali kuseka.

'Ndidzamuonetsa' anaganiza tero fisi tsiku lina. Anayeselera monga maso ake abvutikiratu kuona, anabvala zam'maso zakuda.

Kalulu anapusilatu ndipo anafikiratu pafupi. Ndipo tsiku lina fisi anachotsa dzanja lake ndikugwira kalulu kumakutu. Kalulu anakutumuka kutumuka koma fisi anamuleuza mmwamba ndi panzi atamugwira makutu amene anatalimpha ndikutalimpha mpaka kalulu anakwanitsa kuphuzumuka kukamwa kwa fisi (mano afisi sanali bwino kwambiri nthawi imeneyo) ndikuthawa liwilo kuchoka kumsika, kumzinda wa anthu, kuthawa fisi. Ndicho chifukwa chake muona kalulu ali ndi makutu yatali'.

Msinkhu: Achiambi

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Mapangidwe azinthu ndi mitundu; chikambidwe chakufotokozeria

Zomwe mudzachita: Kuchita zinthu mwaluso, kugwirizana ndi ena

Njira zina zochitiramo nchito:

- Kambani zanyama. Uzani munthu wina wache kuti alembe chithunzi thunzi chake.
- Mugwiritse nchito dothi lowumbira kapena mabotolo akutha nchito ndi zonyamuliramo zakudya kupanga nyama yanu.

Lembani chithunzi-thunzi chamzinda wanu woganizira

Zofunikira: Mapepala ndi maphesulo/ maphensulo yamitundu

Zochita:

- Tengani pepala lalikulu ndi phensulo zikhale pafupi.
- Mupemphe munthu wina akuwelengereni zili munsimu mokweza pang'ono-pang'ono kuti mutseke maso anu ndipo muganizire.

Tsekani maso anu ndipo muwuganizire mzinda wanu. Ganizirani kuti muli kuyenda mumseu wamumzinda wanu wam'maganizo. Ukuoneka bwanji mzinda wanu? Uli ndi manyumba otani? Ndi yotalimpha bwanji manyumaba? Ndi mayendedwe otani amene alimo? Kodi kuli poimilira sitima? Kodi ndi mzinda mamtundu wamsipu umene uli ndi mitengo? Kapena ndi mzinda watsopano uli ndi galimoto zoyenda m'mwamba? Mwamphindi zochepa ganizirani za mzinda wanu.

- Tsekulani maso anu. Lembani chithunzi-thunzi chamzinda wanu. Pangirani komwe zomanga manga zamanyumba zidzakhalire ndiponso zina zomwe mungaikemo muchithinzi-thunzi chanu. Mulembe mwapatali patali poyamba ndipo bwino lake muikemo zotsalira. Mugwiritse nchito zolembera zamitundu ngati muli nazo .
- Mudzaupatsa dzina lotani mzinda wanu?
- Uyang'aneninso mzinda wanu. Kodi pali chomwe mwaiwala? Malo amapemhero kodi? Nyumba yambiri zakale kapena mosungira zambiri yakale? Nanga mtsinje ndi malo amasewera? Kodi anthu angayende-yende munzinga momasuka? Nanga anthu olelala? Ukulitseni mzinda wanu kuti muyikemo izi zonse.



Msinkhu: Achiyambi

Kugwapo kwa akulu/abale: Pakati-kati

Zomwe mudzaphunzira: Kukhazikika kwachilankhulidwe; zamiyeso. momwe mizinda igwirira nchito

Zomwe mudzachita: Kuchita zinthu mwaluso, kupangira, zopanga panga, kuthetsa bvuto

Zapamtima

Zofunikira: Phensulo kapena bopeni ndi pepala ndiponso zamitundu yosiyana

Zochita:

- Lembani m'bali mwazdanja lanu pakati pa pepala.
- Pacholemba chanu mkatì mwa chala chachikulu lembamoni dzina lamtundu omwe mukonda.
- Pazala zotsalira lembamoni chipunziro chakumtima kusukulu, chakudya chakumtima, sewero lakumtima, ndi chinyama chakumtima.
- Kometserani malo otsalira ndi zinthunzi thunzi-zazinthu zakumtima!



Kuonjeza zochita:

- Ikirani zinthu zosiyana-siyana kuti muzilembe pa zala zanu, izi zingakhale zakumtima kapena zina zache monga mizinda ikulu-ikulu, katundu wamnyumba, zomwe mukonda kuchita ndi zina zotere.



Msinkhu: Achiyambi

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Kukhazikika kwachilankhulidwe

Zomwe mudzachita: Kuchita zinthu mwaluso, kugwirizana ndi ena

Njira zina zochitiramo nchito:

- Pemphani munthu wina akulembereni kuzungulira dzanja lanu.
- Muuzeni munthu wina zomwe mukonda.
- Ganizirani zina zakumtima kuti muonjezere.

Yenjamitsani bwato wanu

Zofunikira: Tumatumbo twakale twa pulasitiki kapena mabotolo anatha kale nchito, pepala kapena kansalu, tuminyala

Zochita:

- Pezani thumbo lakale kapena botolo la pulasitiki.
- Pangani bwati wanu, kodi mudzaikaponso ndi mayendedwe am'madzi?
- Yenjamitsani bwato wanu mumgolo wamadzi kapena mukachithaphwi kakang'ono; kodi ayenjama bwanji? Kodi mungamuyendetse pamadzi?
- Tengani minyala. Kodi anganyamule minyala ingati asanamire?



Kuonjeza zochita: Kodi mungapange bwato kuchokera muzinthu zofunikira zosiyana-siyana? Pepala mwachitsanzo? Kodi ichi chingasiyanitse kuchuluka kwamiyala yomwe anganyamule?

Msinkhu: Achiambi

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa / pakati-kati

Zomwe mudzaphunzira: Sayansi (Physics); kalemeledwe kazinthu

Zomwe mudzachita: Kuchita zinthu mwaluso, chigwirizano; zamapangidwe atsopano

Kupita kumsika

Zofunikira: Zinthu zokagulitsa pathandala lanu lamsika, phensulo ndi pepala

Zochita:

- Pezani malo pomwe mngaike thandala lanu lamsika. Lingakhale thebulo kapena malo pansi penapache.
- Ganizirani zomwe msika wanu uzdagulitsa. Kodi ndi zakudya? Zobvala? Mabuku? Kapena zinthu zosiyana-siyana?
- Tengani zinthu zapathandala lanu la msika. Choyamba mufunse kwa achikulire kapena akulu anu ngati ndikoyenera 'kubwerek'a zinthu. Mungagwiritsenso chito miyala, mabatani, tupendelo, masamba amtengo, tumitengo tung'ono-tung'ono monga kuyerekeza zinthu zokulitsa.
- Mugwiritse nchiti tuminyala ndi tumapendelo kuyelekeza monga ndalama. Mupeze kabokosi kakang'ono mosungira ndalama. Muikiretu pafupi pepala ndi phensulo kuti udziwe mitengo.
- Uyikeni m'malo mwake musika wanu. Muyalike zinthu bwino bwino. Lembani mitengo yazinthu patumapepala ting'ono-tun'ono ndipo mutuike pambali pa zinthu zili pamsika wanu.
- Tsekulani msika wanu ndipo muitane odzagula kuti abwere.
- Muchipange chokondweretsa motero kuti nthawi zina simudzakhala nazo zomwe afuna. Mmalo mwake muyeze kuwapatsa zinthu zina. Kapena mukwezeke mitengo ndipo muwauze ogula ndiponso chifukwa chake. Kodi odzagula ailandila mitengo yomwe mwaika lomba.



Msinkhu: Achiambi

Kugwapo kwa akulu/abale: Pakati-kati

Zomwe mudzaphunzira: Kuonjeza ndi kuchotsera ndiponso kuwerengesera potsitsa mitengo, makambidwe azamalonda

What you wil practice: Kulumikizana ndi ena, upandilira malonda, kugwirizana ndi ena, kuchita zinthu mwaluso, kuthetsa bvuto

Mau angati ...?

Zofunikira: Phensulo kapena bopeni ndi pepala

Zochita:

- Lembani chiganizo 'Learning at home is fun'.
- Onani mau osiyana siyana omwe mungapange kuchokera muchiganizo chanu ndipo muyalembe, mwachitsanzo: **Learn, ring, mat, lama, night.**
- Kodi mungapange chiganizo chatsopani kuchokera mumau anu?
- Ganizani chiganizo china ndipo mufunse anthu ena kuti angapangepo mau angati.
- Onani chiganizo chili munsimu chomwe chigwiritsa nchito malembo ones opangira maina (afabeti): '**The quick brown fox jumps over the lazy dog.**'
- Kodi mungapange chiganizo chomwe chingagwiritse nchito malimbo opangira maina amene sagwiritsidwa nchito kwambiri? Mwachitsanzo v kapena j?

Kuonjeza zochita:

- Pangani sewero lamau kusewenzetsa mau.
- Pangani ndi kulemba kankhani kakafupi kugwiritsa nchito mau atsopano.

Msinkhu: Aliyense

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Kukhazikika kwachilankhulidwe; kulemba, masipeling'I, kalembedwe kaziganizo

Zomwe mudzachita: Kuika moyenera, kuika mumdandanda, kuchita mwaluso

Ndikadakhala mtsogoliri wadziko

Zofunikira: Pepala ndi phensulo/bopeni

Zochita:

- Yelekezani kuti ndinu mkulu wa dziko lanu. Ndichiyani chomwe mungayambire kusintha? Kodi mungafune kuchitapo chiyani paizi?
 - ☞ Maphunziro (mwachitsanzo masukulu ndi aphunzitsi).
 - ☞ Malo okhalamo (mwachitsanzo, kuteteza zamoyo).
 - ☞ Zakusamalira umoyo (mwachitsanzo, zipatala, adotolo ndi osamalira owala).
 - ☞ Zapamseu (mwachitsanzo, momwe anthu amayendera Kumalo osiyana siyana).
- Kodi alipo magulu aanthu omwe mufuna kuthandiza?
- Jambulani zolembedwa zili pambalipa ndipo mutsirize ziganizo ndi mau anu.
- Mungaonjezele ziganizo zina zomwe mufuna.
- Chitani zolankhula zamkulu wadziko mwakuwerenga ziganizo zanu mokweza ndipo mwamphanvu.



Ndikadakhala mtsogoleri wa dziko... olemba (dzina lanu)

Ndikadakhala mtsogoleri wa (dziko lanu), ndikada ndiponso bwino lake ndikada

Sembe kunali

Ndikadachotsa

Senbe kunalibe

Ndikanaonetsetsa kuti

Ndine wanu: _____

Msinkhu: Aliyense

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Kukula kwachilankhulidwe; kakambidwe (zoikika zachiwiri)

Zomwe mudzaphunzira: Kuchita zinthu mwaluso, kuganiza mozama, kulumikidzana ndi ena, kukamba pagulu

Kuyankhulana ndi munthu wachikulire

Zofunikira: Phensulo kapena bopeni ndi pepala

Zochita:

- Ganizirani munthu wa chikulire amene mungakonde kumufunsa mafunso anu. Munthuyo angakhale wambaja lanu kapena wa mudela lakwanu.
- Ndizotani zimene zimawakomeletsa? Kodi mufuna kufunsa chiyani? Kodi ndizachibwana kwao? Kuli zosintha zomwe aona? Zimene apitamo pa umoyo wao?
- Lembani mafunso amene mufuna kuti mufunse. Yang'anani mafunso ndipo muyapatse manambala kuti alembedwe mundondomeko imene mufuna kuti mufunsire.
- Yeselerani kufunsa mafunso kwa munthu wina wamkulu kapena mbale wanu wakulu. Ichi chizakuthandizani kudziwa ngati mufunika kusintha chili chonse. Kodi ofunsidwayo anali kuona kuti munakambisana naye mwaubwenzi? Munadzipanga kwambiri? Kodi anali kufuna nthawi kuti akuuzeni zambiri?
- Musinthe mafunso yali yonse yamene muganiza kuti mufunika kusintha mukatsiriza kuyeselera. Kodi mufunirapo mafunso ena? Kodi mufunaachepe? Kodi pali mafunso amene mufuna kusintha?
- Funsani mafunso. Athokozeni ofunsidwawo chifukwa chanthawi yomwe mwacheza nawo.

Kuonjeza zochita: Lembani mafunso monga ndi zowerengedwa zofunika kuti zikaulutsidwe panyumba yamphepo yawailesi yakudera kwanu ndiponso/kapena monga ndi kope ya pepala ya zankhani yakudera kwanu.



Msinkhu: Zaka zopitilira zisanu ndi zitatu (8)

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Kukhazikika kwachilankhulidwe; maphunziro ambiri yabanja kapena yadela.

Zomwe mudzaphunzira: Kulumikizana ndi ena, kuika pamodzi ndi kupangira ndondomeko yamafunso, kuganiza mozama

Njira zina zochitiramo nchito:

- Uzani munthu wina akufunseni inu poyamba kuti mudziwe zomwe mungafunse.
- Lembani mafunso mumalembo yakulu-yakulu kuti chizikhala chapafupi kuona.
- Mafunso anu akhale yafupi-yafupi kuti yasamabvuta kukumbukira
- Mumuuze wofunsidwayo kuti mayankho azikhala yafupi yafupi kuti chikhale chapafupi kuyalemba.

Pangani chitsulu (chida kapena makina)

Zofunikira: Phensulo kapena bopeni

Zochita:

- Ganizirani za chitsulu (chida kapena makina) chomwe mufuna kupanga. Kodi chimachita chiyani? Kapena ndi chinthu chomwe chingathandize anthu? Kodi mungayende nacho paulendo? Kodi ndichopangidwa ndichiyan? Kodi chigwiritsa nchito malaiti?
- Lembani chithunzi-thunzi chachitsulu chanu ndipo nunsu zake zones muzichule maina ake. Kodi nunsu zake zosiyana siyana ndi zachiani?
- Lembani zachitsulu chanu. Kodi mungafotokozele momwe chigwilira nhito? Mungachite nacho chiyani chida chanu?

Kuonjeza zochita:

- Pangani chitsulu chanu kuchokera kuzinthu zotola tola zotha nchito. Pezani mabokosi amene anasewenzetsedwa kale anatha nchito ndi mabotolo apulasitiki mwachitsanzo. Lembanponi panunsu zosiyana siyana zachitsulu chanu ngatimungakonde
- Pangani cholengeza chotsatsa chitsulu chanu. Kodi zotsatsirapo malonda anu ndizotani? Kodi chichita chiyani chomwe chidzafulumizitsa anthu kuti achigule? Kodi chidzathandizira bwanji kufewetsa umoyo wa anthu? Chigulidwa ndalama zingati? Lembani cholengeza chanu chotsatsa malonda papepala lankhani lakwanu.



Msinkhu: Achiambi

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Kukhazikika kwachilankhulidwe; kalembedwe, kupanga mau

Zomwe mudzachita: Kuchita zinthu mwaluso, kuthetsa bvuto, kuganiza mozama, kulumikidzana, kuzindikira zamapangidwe

Chionetsero chazakutha

Zofunikira: Phensulo kapena bolopeni

Zochita:

- Ikani pamodzi zinthu zomwe zinagwiritsiridwa kale nchito ndi zomwe anachotsamo katundu. Izi zikhoza kukhala mabotolo a pulasitiki, tupendelo, mabokosi olimba ndipo amiyeso yosiyana-siyana, zonyamuliramo katundu kusitolo, nsalu zakale ndi zina.
- Mukhozanzo kuona zachilengedwe zina zomwe mungagwirtse nchito popanga chionetsero chazakutha chanu, mwachitsanzo tumitengo tung'ono-tung'ono, minyala, masamba ouma, kapena ngakhale dothi lowumbira kapena matope.



- Ganizirani chomwe mungapange.
Kadoli kodi? kodi chili ndi
mawilo? Kapena ndi kanyumba
kamadimbi? Chili ndi zipupa kodi?
Ganizirani za mainokedwe a
zomwe mufuna kupanga.

Izi ndi zina zazomwe
mungaganizire:

- Lembani chithunzi-thunzi
chamaonekedwe ndipo mupange
ndondomeko ya zomwe
mungafunire kuti chipangidwire.
- Pangani choyelekezera chanu.
- Chiyang'anitsitseni choyelekezera
chanu. Kodi mungaonjezere
bwanji kukoma kwake?
Chingathandizire kuchilimbitsa ndi
chiyani? Nanga kuchithandizira
kuti chiziyenda bwino?



Msinkhu: Achiambi

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Zopanga-panga, masewenzedwe azitsulo,
zamamangidwe

Zomwe mudzachita: Kuchita zinthu mwaluso, kuthetsa bvuto, kugwirizana
ndi ena, kakhalidwe kazinthu

Njira zina zochitiramo nchito:


- Mupempe munthu wina akuthandizireni ndi mapangidwe achoyerekeza
chanu.
- Muwapatse zounikira ndi mau apakamwa zolina kumapangidwe
achoyerekeza chanu ndipo mupemphe wina wache akupangireni.
- Choyerekeza chanu chikhale chapafupi kunvetsa – pangani chiwiya
choikamo chomera, chinthu chomwe chizungulira, sewero lopenda
manambala.

Kupanga mdandanda wazinthu

Zofunikira: Phensulo kapena bopeni ndi pepala

Zochita:

- Ganizirani zinthu zomwe mungapangire mndandanda:
 - ⊕ Nyimbo zomwe mukonda
 - ⊕ Zomera kudela lakwanu
 - ⊕ Zinthu zomwe zimakukondweretsani
 - ⊕ Zinthu zomwe mumachita bwino kwambiri
 - ⊕ Zinthu zomwe mufuna zabanja lanu
- Ganizirani zinthu zomwe siziri zooneka ndi maso monga kuyamikira kapena zinthu zoseketsa.
- Sankhamponi chimozdi ndipo mupange mndandanda wazinthuzo.
- Kodi mndandanda wanu mungaupange kakhala mindandanda ing'ono ing'ono? Mwachitsanzo zomera kumalo kwantu zingapatuldwe motero kuti zodyedwa pazokha ndi zosadyedwa pazokha.



Msinkhu: Aliyense

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Kukhazikika kwachilankhulidwe; kulemba, kupanga mau

Zomwe mudzachita: Kuika zinthu mumndandanda, kuika zinthu molondolana, kuchita zinthu mwaluso

Pangani mapikicha amalo okhalamo akwanu

Zofunikira: Cholembera cha phensulo kapena bopeni ndi pepala, zophikira, zophikiramo

Zochita:

- Dzikonzereni mapepala ndi maphensulo, makamaka zamitundu yasiyana-siyana.
- Ganizirani kuti mukuyenda-yenda kumalo ozungulira kwanuko. Kodi muona chiyani? (manyumba, zomanga-manga ndi miseu komanso mitengo kapena malo ena ache monga machalichi, misikitini kapena malo amasewera).
- Ganizirani kutalimpha kwa miseu ina, kutalimpha kwa mitengo kapena manyumba. Nanga malo omwe mulibe zinthu zilizonse monga posewelera kapena machile? Malo amsika? sukulu? China chilichonse mungachiganizire?
- Sankhani momwe mungapangire mapu yanu. Kodi mudzazipatsa mitundu zinthu zosiyana-siyana? Kodi mudzapanga zizindikiro kuimilira zinthu zina (monga kamzere konyamuka-nyamuka kuimilira mtsinje, kamzera kamsipu kozungulira kuimilira mitengo), kapena mudzangozilemba zithunzi-thunzi zones?
- Lifunika likhale lokula bwanji pepala lanu? Tsamba limodzi? Awiri?
- Chinthu chili chonse chidzafunika chikhale chokula kapena kuchepa motani? Monga masukulu, malo oseweleramo, miseu kapena njira zoyendamo? Msika?



- Pangani mapu. Yapatseni maina malo osiyana siyana kapena pangani zizindikiro ndi kuzipatsa maina

Kuonjeza zochita:

- **Ganizirani:** munthu wachilendo akukufunsani momwe angapitire kumusika kapena kuntsinje. Lembani kapena nenane za mayendedewe. Pezani wina ayione mapu yanu ndipo afunse mayendedewe.
- **Kambani/lembani nkhani yamalo** ena ache mumalo okhalamo anu (sukulu inayamba liti?) kodi malo amasewelera analipo nthawi zones? Kodi kunachitikako choopsy a monga madzi ambiri kapena chimphepo chachikulu Kumalo ao? Nanga zisangalalo? Kuliko mbiri yakale yofunikira? Kuliko nkhani yachipuku yomwe munga nene yokhuza malo ao?
- **Pangani chiyelekezo** chamalo. Mugwiritse nchito zoikamo katundu zakale kapena mabokosi ang'ono-ang'ono omwe mungapeze. Kodi mukhoza kuchipanga moti munthu wosapenya, angakwanitse kuchigwira-gwira ndi kupeza njira yake? Kugwiritsa nchito tunthambo zingathandize.

Msinkhu: Aliyense

Kugwapo kwa akulu/abale: Pakati-kati / kwambiri

Zomwe mudzaphunzira: Kukhazikika kwachilankhulidwe, chikambidwe cham'malo, chilankhulidwe chamalongosoledwe amayendedewe, malo akwanu, zisindikizo zamalo

Zomwe mudzachita: Kuchita zinthu mwaluso, kulumikizana ndi ena, kulemba molingana ndi muyeso, kuyimilira m'malo, kuzindikira zamapangidwe, kuyang'anira

Njira zina zochitiramo nchito:

- Fotokozani zamalo ndipo mufunse wina akuthandizeni kulemba mapu
- Pangani chiyelekezo (m'malo mwa mapu) chamalo,
- Pangani ndondomeko yanyumba yanu kapena chipinda chimodzi chamunyumba mwanu.
- Kambani nkhani zakumalo komwe mukhala ndipo mupemphe wina azilembe.

Pangani kadoli wasokosi

Zofunikira: Sokosi yakale, yoyerá, yayitali, bopeni yaikulu mogwilira kapena choko, mabatani akale, nsingano, kotoní osokera, thonje

Zochita:

- Mupeze sokosi yakale yaitali. Longamoni dzanja mkati ndipo mogwiritsa nchito zala zanu zinai ndi chala chachikulu mupange lembo la C. Ikani chala chanu chachikulu moika kadenene musokosi. Muchiseweretse mpaka chioneke monga mutu ndi pakamwa.
- Gwiritsani nchito bopeni kapena choko kuonetsa pamene padzakhala maso. Chotsani sokosi. Lembani maso awiri kapena sokamponi mabatani pamene munaika chizindikiro chamaso.
- Ikani thonje kupanga tsitsi. Kuchita izi muzidule-dule zolingana nthambo zanu zathonje ndi kuzimanga pakati. Ndipo muzisokelere kusokosi pamwamba pamaso.
- Muikeni madeko kadoli wanu. Mumuike kachisote koyenera kapena mumupangire mulomo wachinthu cholimba kapena nsaru.
- Mupatseni dzina kadoli wanu ndipo muyeselere kumupanga kuti 'akambe'. Mumupange kaoneke woseketsa kapena wodandaula kulingana ndi mwamene tuyendetsera dzanja mkati. Mumupange kuoneka monga wadabwa pamene mufendeza maso ake patali-patali kapena kukalipa pamene mubweretsa maso ake pafupi-pafupi.

Kuonjeza zochita:

- Mupange kadoli wina ndipo muwapange kuti azikambitsana. Kodi mkhalidwe wao ndi otani? Nanga akonda kuchita chiyani? Aonetseri kanema wa akadoli asokosi abanja lanu.



Msinkhu: Achiambi

Kugwapo kwa akulu/abale: Pakati-kati

Zomwe mudzaphunzira: Kulemba zithunzi-thunzi, kukambirana, kukhazikika kwa chilankhulidwe

Zomwe mudzachita: Kugwirizana ndi ena, kuchita zinthu mwaluso, kuchita nchito kusewenzetsa zomwe zipezeka.

Nsolo kapena sewero lazowerenga lolinga nalo

Zofunikira: Phensulo kapena bopeni ndi pepala

Zochita:

- Kodi ndimasewera otani amene mumawerenga zoseweretsa mdziko lanu? Kodi alipo masewera amene mumagwiritsa nchito tuminyala tung'ono tunng'ono, kayela ouma, njele kapena zowerengetsera zina ndiponso muchitira pathabwa (molingana ndi zimene aonetsa munsi)?
- Musewera bwanji sewero lanu? Kodi tuyadziwa malamulo asewero limenelo? Ngati simudziwa, kodi mungapeze munthu amene angakuphunzitseni?
- Ngati mulibe 'thabwa' logwiritsa nchito kodi mungapange posewelera pansi? Mukhoza kupanga tumiboo tung'ono-tung'ono pansi ndipo mugwiritse nchito tuminyala tungono-tung'ono.
- Sewerani sewero. Ngati mufuna kusewera awiri mupeza munthu wina musewere naye. Chimene chilipanga kukhala sewero labwino ndi chiyani? Ndiukatswiri otani umene mukuonetsa?





Kuonjeza zochita:

- Kodi mungalembe zounikira zasewero lanu? Ganiziranu zounikira kwa munthu amene akalibe kusewerapo sewero limeneli.
- Mungapange sewero lazowerenga lanu? Phunzitsani munthu wina aliyense sewero lanu. Malamulo asewero ndi otani?

Msinkhu: Aliyense

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Zamanambala, kukhazikika kwachilankhulidwe, (zounikira)

Zomwe mudzachita: Kugwirizana ndi ena, kuthetsa bvuto, kulumikizana ndi ena, machitidwe azinthu

Kuyang'anira zachilengedwe

Zofunikira: Phensulo kapena bopeni ndi pepala

Zochita:


- Mupite panja ndipo muganizire chomwe mufuna kuyang'ana. Chikhoza kukhala kadoyo monga kachiduwi-luwi kakupanga ukonde wake kapena kanyerere kakunyamula chakudya mkamwa mwake. Chingakhale kanthu kouluka monga balaula, kambalame kapena njuchi zikutenga usinda. Kapena mungayang'ane mitengo ndi mithunzi yomwe ipanga kapena kuwala pamadzi mumtsinje.
- Penyererani mwamphindi khumi ndi zisanu (15) ngakhale kupilirapo ndiponso muone zonse zomwe mungakwanitse. Onani momwe chiyendera, mabala-mabala alionse pathupi kapena mitundu, (mitundu yowala yachiopsyezo kapena mitundi imene igwirizana ndi pomwe chakhala). Kodi mungachifotokoze?
- Mudzifunse mafunso ena: Ndichachikulu bwanji? Chili ndi miyendo ingati? Chiyenda bwanji? (mofulumira, pang'ono pang'ono, mosaoneka bwino, monyada). Chikupita kuti? Ndi chiyani chili munjira mwake, chikufuna kuchita chiyani kapena kupanga chiyani?





Kuonjeza zochita:

- **Lembani** chithunzithunzi chazomwe mwaona
- **Mupeze** uthenga wina okhuzani ndi zomwe munaona. Mufunse wina amene adziwa zazinthu izi ndipo muganizire mafunso amene mungamufunse. Kodi chinyamacho/chidoyo chikudya chiyani? Pali mitundu ingati? Zimapeza bwanji chakudya? Kodi zimakhala pamodzi kapena chili chonse chokha? Kodi zimakhala bwanji ndi ana? Kodi zimayenda m'malo m'malo?
- **Pangani cholembamo chazachilengedwe.** Ichi chingakhale pepala pamene mungalembe malembo kapena zithunzithunzi zazimene mudzaona tsiku ndi tsiku. Ngati mungaone zinthu zolingana kwamasiku ambiri (monga mithunzi yamitengo kapena liliwa limene latseguka kapena mtsinje), muikeko nzeru kuyang'anira zomwe zidzachitika pamasiku osiyana. Kodi kuli tudoyo tosiyana-siyana tomwe tumabwera kudzakhala paliluwa? Nanga mumtengo? Kodi mbalame zimabweramo kapena masamba ake amasinthia? Ikukula Kodi? Nanga mumtsinje? Kodi muli nsomba zosiyana-siyana kapena tudoyo m'kati kapena m'mbali mwake? Kodi mtundu wamadzi umasinthia?



Msinkhu: Aliyense

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Kukhazikika kwachilankhulidwe; chilankhulidwe chofotokozena, sayansi: zachilengedwe ndi zaumoyo

Zomwe mudzachita: Penyetsetsani bwino bwino. Kuphunzira zomwe mukupenya. Kudekha mtima, kuganiza mozama, kulumikizana ndi ena

Njira zina zochitiramo nchito: Ngati mupeza bvuto kouna, mugwiritse nchito nzeru zina (osati kupenya chabe) kuti munvetsetse zachilengedwe. Munvetsere ndi makutu, mununkhize ndi mphuni ndipo mugwire dothi, mitengo ndi zomera pamene muli. Fotokozerani zomwe mukununkhiza, mukuzinva ndiponso zomwe mukuzigwira. Mumuuze zofotokoza zanu munthu wina wache kuti akulemberani.

Nyimbo yatsopano, maimbidwe akale

Zofunikira: none

Zochita:

- Ganizirani nyimbo yomwe aliyense adziwa ndipo ndiyopusa kuimba
- Muikemo mau atsopano mumaimbidwe omwewo. Mungapange nyimbo pachili chonse chomwe mufuna, mwachitsanzo, momwe titsukura mano mkamwa, mkhalidwe unakukondweretsani munkhani, kapena china choseketsa chimene chinachitika.
- Muwaphunzitse ena nyimboyo. Ngato mufuna mungaikemo kuyeselera.
- Apa pali chitsanzo cha nyimbo ya '**Kodi mwasamba**' inaimbidwa mumaimbidwe a nyimbo ya 'kodi mwalembo'

Oyamba: Kodi mwasamba

Onse: Inde

Oyamba: Kodi mwapesa

Onse: Inde

Pamodzi: Bwerani mudzaone, bwerani mudzaone

Tasamba, tapesa kuoneka aukhondo,

Bwerani mudzaone tayera .



Msinkhu: Achiambi

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Kukhazikika kwachilankhulidwe, maimbidwe, malembo amasilabo, mau mumaimbidwe.

Zomwe mudzachita: Kusintha zinthu, kuchita zinthu mwaluso.

Nthano yosokonezekwa

Zofunikira: Bopeni phensulo ndi pepala

Zochita:

- Onani nthano yosokonezekwa (yopeka) munsimu. Nthanoyi inalembedwa mchinyanja ndipo muikire nzeru ku mau osokonezekwa osayembekezereka ali mkati.


Kambuma kanadya mbuzi kwambulanda

Kwambulanda kumene kuli kambuma
 Kambuma kanadzipeza pakati pambulu
 Kwambulanda komwe mbulu zilibi mapiko
 Mbulu inaluma mbuzi kwambulanda
 Kwambulanda kumene kambuma kanalowa mumbatata
 Kwambulanda komwe mbuzi ikudya mbatata
 Kwambulanda, kwambulanda, kwambulanda
 Mbuzi inatupa mimba Kwambulanda
 Kwambulanda mbuzi inafa
 Kambuma kanadya mbuzi kwambulanda
 Kwambulanda kwambulanda kwambulanda

- Mukatsiriza kuwerenga, mulembe mndandanda **wamau onse osokonezeka** amene anagwiritsidwa nchito munthanoyi.
- Ndi liu liti losokonezeka lomwe mwakonda kwambiri ndipo ndi chifukwa chiyani?
- Kodi muli nazo nthano zosokonezeka m'mudziko/chilankhulidwe chanu?
- Lembani matanthauzo yamau ali pamwamba amene adzasokoneza anzau.
- Lembamoni mumpata osiyidwa mau anu odzipagira amene afotokoza zochitika/zonveka:
 - ⦿ Mphepo mumitengo
 - ⦿ Mwamene zililira zala pabolodi wakuda
 - ⦿ : mwamene chichitira chitosi chambalame pakugwa pansi munjira
- Pangani mau anu anu asanu (5) ndi matanthauzo ake.
- Tsopano lembani nthano yanu yosokonezeka kugwiritsa nchito mau anu osokonezeka. Simufunika kuti mpakana mau onse muwasewenzetse. Sankhani amene mukonda kwambiri ndi amene anveka bwino kwambiri pamodzi.

- Mungagwiritse nchito 'pama Ning' Nang'I Nong'o' kukhala ngati chilimbikitso. Muyesetse kuyamba ziganizo zanu ndi mau olinganako monga:

- Pamene pa
- Kumene ku ...
- Ndipo ana ...
- Zonse zina...



Msinkhu: Zaka zakubadwa 8 kupita kutsogolo

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Kukhazikika kwachilamnkulidwe, matanthauzo, kupanga ziganizo, mau olingana mamvekedwe ndi mamvekedwe olondolana mwaluso.

Zomwe mudzachita: Kuchita zinthu mwaluso, kulumikizana, kupanga tanthauzo.

Njira zina zochitiramo nchito:

- Mungakambe nthano yanu pakamwa kapena mungafunse munthu wina kuti akulembereni
- Lembani nthano yamizera iwiri chabe

Bzalani mbewu ndipo muionelere ikule

Zofunikira: Mbewu, dothi, madzi, kamtengo, cholembera chooneka

Zochita:

- Sankhani mbeu yomwe mufuna kubzala ndi kukulitsa. Kayela, nyemba kapena mbeu zina? Kodi mufuna kubzala ndi kukulitsa zomwe mufuna kuti mukadye? Fufuzani mbeu zimene zimera ndi kukula bwino nyengo ino yachaka ndi mbeu zomwe zilipo.
- Ganizirani komwe mungabzale mbeu zanu. Mupoto wamaluwa kapena pansi? Ngati ndi mudothi, sankhani malo pamene sipadzakhala msokonezo wanyama. Mufufuze malo abwino obzalapo mbeu zanu. Kodi ndi malo ochinjirizidwa? Mumene muli mthunzi, kapena padzuwa?
- Mubzale mbeu zanu pamalo pamene palibe udzu. Bzalani mbeu ziwiri kapena zitatu zamtundu wolingana pamalo mamodzi kuchitira kuti mwina ina siidzamera (kukula). Muithilire madzi mokwana.
- Pangani dzina lachomera chanu. Lembani dzina lachomera chanu pakamtengo ndipo mukaimike mdothi pafupi ndi mbeu zanu.
- Thilirani tsiku lililonse kapena pafup pafupi kuti dothi likhale ndi madzi nthawi zonse.

Kuonjeza zochita:

- Tsiku lililonse muziona makulidwe. Muzilemba zamakulidwe ambeu zanu. Mbeu zikamera kutulukira kubwalo muzipima msinkhu wake tsiku ndi tsiku. Papita masiku angati kuti zipange masamba? Maluwa? zipatso? muzilemba zonse zomwe mukuona.



Msinkhu: Aliyense

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Kulima chakudya, zachilengedwe, kusamalira chomera

Zomwe mudzachita: Kupenyelera, kuthetsa bvuto

Kuwerenga pamodzi

Zofunikira: Buki lankhani (kapena muwerenge nkhanzi patsamba lotsatira)

Zochita:

- Munthu kapena m'bale wamkulu angamuwerengere mwana nkhanzi kapena mwana angamuwerengere mbale wake wamkulu. Nthawi zina chimakometsera kuchita wina wawerenga winanso wawerenga pamene wina akumvetsera.
- Sankhani nkhanzi (kuchokera mubuku) imene nonse awiri mukonda kapena mupange nkhanzi yatsopano. Ingakhale nkhanzi yazoona kapena yopeka yonveka bwino.
- Kumbukirani kusintha mau anu pamene mukamba mkhani. Kodi mungapange bwanji mau a mkango, mudala okalamba, kalulu amene wayopa?
- Nthawi zina mungapume munkhani ndipo mungafunse kiti 'kodi muganiza kuti ndi chiyani chidzatsatirapo?'. Pamodzi kambiranani zomwe muganizira kuti zidzachitika mundime yolondolapo yankhani.
- Patsamba lotsatira pali nkhanzi imene mungawerenge pamodzi. Muwerenge gawo leni leni lankhani, mupume mukalibe kuwerenga gawo lothera ndipo tuyese kuganizira momwe idzathera.
- Werengani matsirizidwe ankhani. Kodi munaganizira zoona? Kodi mungapange mutu wake wankhani?

Kuonjeza zochita:

- Kodi mungasewelere pamodzi sewero lankhani yomwe mukonda? Sankhani mbali yomwe mudzasewera ndipo musewere nkhanzi. Muwaonetse sewero lankhani abale ndi alongo ena ambanja lanu.

Nkhani yoyanba: Tembo, kanjobvu

Osapita kumtsinje' mai wanjobvu anali kumuza Tembo mwana wake. 'Kuli ching'ona chachikulu ndipo chidzakudya.' Tembo anali kufunitsitsa kuona. Nanga ng'ona inali chiyani? Palibe anali kumuza. Motero, anapita kumtsinje. Anaimilira pamgumira wamtsinje. Anafendera pafupi kwambiri. Koma chomwe anali kuona ndi nkope yake mumtsinje. Anafenderakonso pang'ono ndipo mwadzidzidzi ng'ona inaonekera ndi kukamwa kokanganuka ndipo kwapi! Inamunyamula Tembo champhuno. 'Ndithandizeni' anakuwa Tembo. Amai ake anabwera akuthamanga, anamugwira mchira. Azibale ake anabwera akuthamanga ndipo anamugwira makutu, ndipo anadonsa mwamphamvu koma ng'ona siinamusiye. 'Tithandizeni' anakuwa ndipo mosachedwa aliyense mnkhalango anali kudonsa.

Kutsiriza:

Anaidonsa kumchira ndipo unatalimpha monga nthambo, anadonsa makutu ndipo yanakula, ndipo mphuno yake inatalimpha kwambiri. Anadonsa ndi kudonsa mpaka pothera ng'ona inamusiya. Aliyense anagwera pamwamba pamnzake paudzu. Tembo anamasuka. Koma zomwe zinahitika kumchira wake wopombekana ndi makutu ake ang'ono-ang'ono, and MPHUNO yake? ndicho chifukwa chake mpaka lero, njobvu zili ndi mphuno zitali-zitali zochedwa chitamba ndipo makutu akulu-akulu monga mayani yakabichi.

Nkhani yachiwiri (2): Chidiso mumtolo

Kudziko lina lache kunali mudzi odziwika ndi dzina lakuti Kumva. Pamudzi wa Kumva anthu anali kugwirizana kwambiri koteru kuti chili chonse anali kuchitira pamodzi. Nthawi ina kuthengo pafupi ndi mudzi wa Kunva kunabwera mkango ndipo unali kufuna kuti udye anthu. Anfumu atadziwa zaichi anaiza anthu ao kuti pasakhale ngakhale mmodzi amene adzapita yekha kumunda.

Mkango unakhala masabata awiri kulindilira munthu amene adzapezeka yekha kuthengo kuti umudye koma sanaoneke. Unayamba kufendera kumudzi mang'ono-pang'ono mpaka unafika kumbali kwa mudzi. Mkango unalowa pakati pamitolo yaudzi inali pamtengo pakati pamudzi kuti anthu asauone.

Madzulo anthu anayamba kubvina pafupi ndi pomwe panali udzi. Mwamwai kamwana kakang'ono kanaona diso lamkango mumtolo waudzu ndipo kanayamba kuza anthu mwanzeru kuti 'chidiso mumtolo' koma anthu sanamuike nzeru. Koma kamwana kanapitiriza kuwauza anthu kuti 'chidiso mumtolo'.

Kutsiriza:

Komabe anthu sanamve ndipo anapitiriza kusangalala ndi kubvina. Mwadzidzi mkango unalumpha kuchoka mumitolo yaudzi ndipo anthu onse anabalalika kuthawa. Zinali zachisoni pamene amfumu anaitanitsa msonkhano m'mawa mwache anapeza kuti nkhalamba imodzi inagwidwa ndi mkango. Ndipo anthu onse analira.

Msinkhu: Aliyense

Kugwapo kwa akulu/abale: Kwambiri

Zomwe mudzaphunzira: Kukhazikika kwa chilankhulidwe, kupanga nkhani, kuganizira, kuchita sewero lankhani

Zomwe mudzachita: Kuchita zinthu mwaluso, kugwira nchito pamodzi ndi ena, kugwirizana, kunvetsera

Kufuna-funa zakufa kale

Zofunikira: Pepala ndi phensulo

Zochita:

- Musewero la Kufuna-funa zakufa anthu ayembekezereka kufuna funa ndi kupeza zinthu zomwe zili pamndandanda wanu. Mungafune-fune munyumba kapena panja. Ngati musewera pamodzi ndi ena, amene adzayambire kupeza zinthu zonse zili pa mndandanda ndiye wapambana.
- Uoneni mndandanda wa zinthu. Painu nokha kapena ndi anzanu, kodi mungakwanitse bwanji kutenga zinthu zonse zili pamndandanda?

- Chamtundu wobiliwira
- Chofewa
- Zinthu ziwiri zopangidwa ndi mapulanga
- Chonzuna
- Zinthu zitatu zoyambira ndi P
- Chowala
- Chosewenzetsa pophsyera
- Chomwe mukonda kwambiri

- Ngati muchita sewero lakufuna-funa ndi munthu wina, linganizani zinthu zosiyana siyana zomwe mwatenga.

- Pangani mndandanda wanu tsopano. Kugwiritsa nchito mau ofotokoza zamaina (yofewa, yonzuna, yowala) ndi mitundu ndi chiyambi chabwino. Penyani chitsanzo china chili pamwamba ndipo muone ngati mungapange mndandanda wanu wazinthu khumi (10) zofunika kupeza.
- Lembani mndandanda wanu ndipo mufunse munthu wina apite akazipeze zinthuzo.



Msinkhu: Aliyense

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Kukhazikika kwachitundu (mau ofotokoza ndi maina), kuwerenga zinthu

Zomwe mudzachita: Kuchita zinthu mwaluso, kuthetsa bvuto, kugwirizana

Njira zina zochitiramo nchito:

- Musankhe zinthu zimene zipezeka muchipinda chimodzi chabe munyumba mwanu
- Muziloze ndi chala zinthuzo ndipo mupemphe muntu wina akutengereni
- Muuzeni wina (uzani munthu wina) zinthu kuti akulembereni mumndanda

Nambala yobisika yachisinsi

Zofunikira: Phensulo kapena bopeni ndi pepala


Zochita:

Pali njira zambiri mopangira nambala yanu-yanu yachisinsi yobisika.

- Mungaikepo nambala pa lembo lililonse lamu afabeti wanu koma muyambire ndi nambala yayikulu kwambiri ndipo popereka manambala muziyenda chakumbuyo. Mwachitsanzo chinyanja chili ndi malembo 24 (m'malo mwa 26 chifukwa q ndi x mulibe mchinyanja) motero kuti **a=24, b=23, d=22** mpaka tero. Kodi manambala awa atanthauza chiyani? **11 24 12 23 24 13 24 22 17 16 7 16 11 7 16**
- Mungaike malembo pamalembo anzake amuafabeti koma musunge mdondomeko yake, mwachitsanzo **a=h, b=i, c=j, d=k, e=l, f=m** mpaka tero.

a	b	c	d	e	f	g	h	i	j
r	ɔ	≈	◊	ε	ɔ	Ⅱ	迢	⊖	◎
k	l	m	n	o	p	q	r	s	.
↙	≈	▷	₩	○	ε	₩	↗	□	.
t	u	v	w	x	y	z			
△	♀	♀	ω	₩	♀	□			

- Mukhozanzo kupanga zizindikiro zatsopano kuimilira lembo lililonse lamuafabeti monga zaonetsa muchitsanzo. Ngati mufuna kupanga zizindikiro zanu mudzifunse mafunso awa:
 - ⦿ Kodi nambala yanga yachisinsi yobisika idzalembewa kuchokakudzanja lamanzere kupita kudzanja lamanja? Kapena kuchoka pamwamba kupita pansi?
 - ⦿ Kodi zidzawerengedwa molingana zizindikiro ndi malembo amuafabeti? Kapena zizindikiro zingapo kuimilira lembo limodzi? (ichi chimathandizira kukhale chobvuta kuti munthu a lowelera nambala yanu yachisinsi yobisika)
- Kodi mungapange mau muchinyanja kuchokera pazizindikiro zomwe mwapatsidwa pamwambapo?
- Tengani bopeni kapena phensulo lanu ndi pepala zikhale pafupi. Lembani nambala yanu yachisinsi yobisika mwathunthu. Lembani mauthenga achisinsi ndipo muone ngati ena angakwanitse kuilowelera.



Msinkhu: Aliyense

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Kukhazikika Kwachilankhulidwe; kulemba, malembewa amau

Zomwe mudzachita: Kuchita zinthu mwaluso, kulumikizana ndi ena, kuthetsa bvuto

Maonekedwe ndi mapangidwe azinthu muchilengedwe

Zofunikira: Tumitengo ndi tuminyala tung'ono tung'ono

Zochita:

- Tulukirani panja. Ndimaonekedwe otani ndi makhalidwe azinthu osiyana siyana amene mukuona muzolengedwa zamdziko? Komanso muyang'ane zinthu zomwe zichokera kuzachilengedwa zomwe muli nazo munyumba mwanu, monga zipatso ndi ndiyo zamasamba.



- Kodi ndimakhalidwe angati ndi maonekedwe osiyana-siyana achilengedwe amene mungachule? Kodi mungapeze chinthu:
 - ☞ Chimene mukaika mzela pakati-kati chipangika magao awiri olingana?
 - ☞ Chili ndi maonekedwe ochita monga kanthambo kamodzi kazungulira kuchoka kunsi mpaka kumwamba?
 - ☞ Ndichozungulira kapena chili ngati dzila maonekedwe ake?
 - ☞ Chioneka monga chibwerezera maonekedwe amodzi ndi amodzi kambiri-mbiri
 - ☞ Chioneka monga nyenyezi kapena chili ndi maonekedwe monga mtima

- Kodi munaonako mwamene masamba ena aonekera monga tumitengo tung'ono tung'ono? Kodi mungalipeze tsamba lotero? Kodi mungawerenge nambala ya tuzogawo tung'ono tung'ono pa tsamba limodzi?
- Tengani tumitengo ndi tuminyala tung'ono-tung'ono. Ndimapangidwe otani ena omwe mungapange kuchokera kwa izi?
Kodi mungapange kanthu:
 - ⦿ Kali ndi mbali ztatu (3) kapena zinai (4) zonse zolingana?
 - ⦿ Kali ndi mbali zinai (5),
 - ⦿ Kali ndi mbali zisanu ndi imodzi (6),
 - ⦿ Kali ndi mbali zisanu ndi zitatu (8)
- Kodi mungapange chinthu chomwe ndi chokhazikika ndipo chionekera mungodya zitatu kugwiritsa nchito tumitengo ndi tuminyala twanu? Kanyumba koimilira kapena kabati mwachitsanzo?



Msinkhu: Aliyense

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Maina amaonekedwe azinthu, mau yofotozera maonekedwe azinthu, kuwerenga

Zomwe mudzachita: Kuchita zinthu mwaluso, kuthetsa bvuto, kugwirizana, kuyang'anira

Nkhani yozungulira

Zofunikira: Phensulo kapena bopeni ndi pepala

Zochita:

Mukhoza kuchita izi ndi anthu atatu kapena ochulukirapo. Mukhale pamodzi mozungulira

- Munthu mmodzi adzayamba nkhani, mwachitsanzo, "Panali kamtsikana kena kamene sikanali kugona. Kanatembenuka ndi kutembenuka koma osabwera tulo"
- Imani pomwepo. Funsani munthu wachiwiri kuti apitiliza nkhani ndichiganizo chimodzi kapena ziwiri, mwachitsanzo,
"Kanali kungoyang'ana mwezi waukulu wozungulira. Mosachedwa kunaonveka ngati kunachoka chinthu kumwezi kupita kunali iko. Analu matanda owoneka bwino amene anabwera pansi, pansi, pansi, mpakana pawindo yake".
- Pelekani nkhani kwamunthu wachitatu kuti apitirize kapena muibweze kwaoyambilira ngati pali chabe anthu awiri okamba nkhani. Kodi nkhani yanu mungaikambe kwanthawi yayikulu bwanji?
- Mufunse wina aithetse nkhani pamene monse mwakambako kawiri kawiri.
- Malamulo ankhani yozungulira ndi akuti:
 - ⊖ Gwiritsani nchito malingaliro anu, chili chonse chitheka!
 - ⊖ Ipelekeni kutsogolo nkhani (simunganene, anayenda pamatanda kupita') ndikuimilira pamene po, muyenera kukamba zambiri pang'ono 'anayenda kukwera matanda mpaka anafika pamwamba ndipo anaona')
 - ⊖ Osakamba nkhani yonse, nthawi zonse muone kuti otsatirapo ndiye apitiriza.

- Mungasankhe gawo lilionse lankhani. Ingakhale yachinthu chazoona (monga madyelero kapena ulendo) kapena chinyama kapena nkhani yokondweretsa yam'malingaliro anu.



Msinkhu: Achiambi

Kugapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Kukhazikika kwa chilankhulidwe; kupanga nkhani ndiponso kupanga malamulo ankhani: Zomwe mungachite ndi zomwe simungachite munkhani mukaiyamba.

What you wil practice: Zomwe mudzachita: Kuganiza mothananga, kuchita zinthu mwaluso, kulumikizana ndiponso kuchitira zinthu pamodzi.

Njira zina zochitiramo nchito:

- Ikani muchola zinthu zing'ono-zing'ono zokwanira ngati khumi (10) zapanyumba panu chili chonse chimene mungapeze, mwachitsanzo kapu, kamwala, kansalu ...); mmodzi mmodzi muzichotsa zinthu mchola chimodzi-chimodzi, nthawi ili yonse pamene muchotsa chinthu muchola muchigwiritse nchito kuwonjezera chiganizo chatsopano kunkhani . Mwachitsanzo, pamwamba patanda anaona kapu, yooneka bwino ndipo inali yosefukira ndi madzi odabwitsa agolide ...'
- Lembani nkhani ybwino mwapaga pamodzi. Muikemo mau ofotokoza zazinthu ndoponso chilankhulidwe chofotokozena kuipanga ikhale yomveka bwino.

Thokozani ngwazi yakwanu

Zofunikira: Pepala ndi phensulo

Zochita:

- Ngwazi angakhale munthu aliyense amene anathandiza anthu kudera lakwao kapena anakhala nazo mphamvu zopitiriza kuchita chinthu ngakhale kuti anapeza zobvuta. Aliyense angakhale ngwazi. Kodi alipo amene mudziwa wotere?
- Ganizirani zagwazi yakwanu. Kodi ndani? Anachita chiyani? Ndichifukwa chiyani muwakhumbira?
- Kodi mungafune kuithokoza bwanji ngwazi yanu? Kuipangira chithunzi thunzi chake, kuipangira chikongwani kapena nyimbo yosekelera zimene inapambana? Kalata yazikomo kapena mphatso yamtundu wina? Kapena mwina mufuna mukangonena kuti 'zikomo'.
- Pangani mphatso/lembani kalata ndipo mupeze njira yabwino yoperekero kwa ngwazi yanu. Pemphani munthu wamkulu kapena mbale wanu wamkulu kuti akuthandizeni.



Msinkhu: Achiambi

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Kukhazikika kwachilankhulidwe

Zomwe mudzachita: Kulumikizana ndi wna, kuchita zinthu mwaluso, kukhazikika kwachifundo ndi mtima wothandiza

Kufuna-funa chokoma

Zofunikira: Phensulo kapena bopeni ndi pepala

Zochita:

Kufuna funa chuma ndi sewero mwamene osewera amafuna funa chinthu china chobisika **kulondola zounikira**. Chounikira chili chonse chimene mwasewenzerapo chikulongozani kwa chotsatira mpaka muchipeze chokoma chanu. Chokoma cheni-cheni chapotsirizira chingakhale chili chonse chamwe mungakonde – kanthu kakang'ono kokondweretsa kapena chinthu chomwe mungadye (mungoonetsetsa kuti ngati mwachibisa chinyama china chisafikepo).

- Ganizirani amene mufuna kuti muchitire kufuna funa chokoma – mubale wanu wamng'ono kapena wamkulu? Munthu wachikulire? Mudzafunika kuti mulembe zounikira zoyenera msinkhu wao wakubadwa ndipo kuti amvetsetse (onani zitsanzo munsi).
- Ganizirani komwe mufuna kuchitira sewero la kufuna funa chokoma – mcati mwanyumba kapena panja kapena konse mcati ndi panja? Kodi sewero lidzayambila kuti ndipo lidzatsirizira kuti?
- Sankhani malo (mumalo mwamene mudzaika zounikira) yasewero lakufuna-funa chokoma. Mumtengo waukulu, Mukabati munyumba, kapena chounikira chingakhale ndi wabanja wina amene siali pagulu lamasewera. Malo asanu ndi atatu (8) angakhalnire. Muwalembe malowo ndipo muwapatse manambala.
- Lembani chounikira chamalo alionse papepala lake. Muonetsetse kuti aliyense amvetsetsa zounikira zimenezi koma zisakhale zapafupi kwambiri! Mwachitsanzo:
 - ⌚ Chounikira: Ndili ndi lalanje lokoma, madzi ake onzuna (malo: mumtengo wamango)
 - ⌚ Chounikira: Kwamene mumalota usiku (chounikira: bedi)

Mukhozanso kugwiritsa nchito anagilamu (pamene mulenba mau koma mosokoneza sokoneza) mwachitsanzo:

↪ Chounikira: ogoml dwamzai (malo: mgolo wamadzi)

- **Zipatseni manambala zounikira** ndipo mupeteke tumapepala koteru kuti nambala yokha ndiyo izionekera
- **Sungani chounikira choyamba ndipo mukabise zounikira zina** mumalo mwake kulondola mundandanda – mudzagwiritse nchito paja munalemba kuti zikukumbutseni kumene mufunika kubisa. Pamene pali chounikira choyamba ndi pomwe mudzabisa chounikara chachiwiri, pali chounikira chachiwiri ndipamene mudzabisa chounikira chachitatu mpaka tero. Chounikira chotsirizira ndi pamene mudzabisa chokoma chanu.
- Ngati osewera apitilira pammodzi tuyenera kugwirizana pamalamulo. Lamulo lingakhale mwachitsanzo:
 - ↪ Tifunika kuyembekezana tikalibe kupita kuchounikira china.
- **Perekani chounikira choyamba.** Muyende yende nawo ochita masewera kuti muwathandize ngati sakunvetsetsa chounikira,

Msinkhu: kupitilira zaka khumi (10)

Kugwapo kwa akulu/abale: Pakati kati

Zomwe mudzaphunzira: Kukhazikika kwa chilankhulidwe; kulemba, kupanga mau

Zomwe mudzachita: Kuika moyenera, kuika zinthu milondolana, kuchita zinthu mwaluso, kuganiza mozama, kulumikizana ndi ena, kuchitira pamodzi, kuthetsa nchito

Njira zina zochitiramo nchito:

- Mupemphe munthu wina akuthandizeni kulemba zounikira
- Mulembe zofunikira zitatu (3) kapena zinai (4)
- Musachite masewera akufuna-funa chokoma ‘moyeselera’ poyamba koma zindikirani kuti chounikira chili chonse chingakulongozeni kumene kuli chokoma china – ichi chimathandizira kupeputsa makonzedwe.

Mafunso makumi awiri

Zofunikira: Palibe

Zochita:

Nchito iyi imachitika bwino ngati pali anthu kuchokera pa awiri (2) kufikira asanu (5) koteru kuti aliyense akhala ndi mpata wofunsa funso.

- Mungasankhe aliyense mugulu lanu kuti akayambe. Mwachitsanzo, wamng'ono kwambiri kapena amene tsiku lake lobadwa linapita lomba pano.
- **Musankhe munthu, malo, kapena chinthu.** Ganizirani munthu kapena chinthu chimene mudziwa bwino kwambiri zake kuti muyankhe mafunso apaicho. Ngati mwasankha munthu, akhale wakuti akali moyo kapena anafa kale palibe kanthu, kapena ndi woganizira chabe (wamnkhanu ina yache). Muonetsetse kuti musankha munthu, malo, kapena chinthu chimene ambiri mugulu lanu achidziwa.
- Ena mufunse mafunso amene afuna yankho ya inde kapena ai. Muyambe ndi funso lomwe lifuna yanko yakuti 'inde' kapena 'ai'. Mwachitsanzo:

⊖ "kodi ndi munthu?"

⊖ "kodi ndi malo?"

⊖ "Kodi ndi chinthu?"

⊖ "kodi ndi chazoona kapena chopeka mmutu?"



- **Muzisinthana kufunsana mafunso ofuna yankho ya inde kapena ai.** Muonetsetse kuti aliyense pamasewera ayankhako mpakana funso limodzi. Ngati wina afunsa funso lomwe yankho yake siyikhala "inde" kapena "ai", mumuuze afunsenso mpaka yankho ikhale "inde"

kapena "ai". Mwachitsanzo, munthu sangafunse kuti, "ali ndi zaka zingati?" koma akhoza kufunsa kuti "kodi zaka zao zakubadwa zipitilira makumi asanu (50)?"



■ **Pamene mupitiriza muzifunsa mafunso olunjika.**

Kumbukirani mafunso amene afunsidwe kale mukalibe kufunsa mafunso atsopano. Mwachitsanzo, ngati wina wafunsa kale zakukula kwazinthu, mungafunse zamitundu kapena kuti chinapangidwa ndi chiyani.



■ **Mupitirize kusewera mpaka mufikitse mafunso makumi awiri (20) kapena wina adzapereka yankho yazoona.**

Werengani nambala yamafunso pamodzi. Ngati gulu lafikitsa mafunso makumi awiri (20) ndipo akalibe guganizira munthu, malo kapena chinthu, auzeni chinthucho. Ngati wina waganizira yankho yazoona mafunso akalibe kukwana makumi awiri (20) ndiye kuti sewero latha.



■ **Amene waganizira chazoona ndiye adzalondolapo kupita.**

Ngati kulibe amene waganizira chazoona wina aliyense amene afuna angalondolepo. Mulole kuti aliyense akhala ndi mpata woganizira chinthu. Ngati aliyense apatsidwa mpata mupanga sewero kuhala laonse ndipo chipangitsa kuti aliyense akhale ndi chisangalalo!



Msinkhu: Aliyense

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Kukhazikika kwa chilankhulidwe; magawo-magawo

Zomwe mudzachita: Kulumikizana ndi ena, kuganiza mozama, kuthetsa bvuto

Njira zina zochitiramo nchito:

- Mafunso akhale olunjika kuchinthu chimodzi, mwachitsanzo 'nyama', 'chakudya' kapena 'anthu okondedwa kwambiri'. Auzeni ochita sewero gawo limene mwasankha
- Muzisewera mumagulu ya awiri-awiri kuti muzithandizana inu awiri.
- Mungaonjeze mafunso kupitilira pa makumi awiri kuti mukhale ndi mpata opeza yankho yazoona.

Kalata kwa aphunzitsi

Zofunikira: Pepala ndi phensulo

Zochita:

- Tengani phensulo ndi pepala zikhale pafupi.
- Ganizirani zomwe mufuna kukamba kwa aphunzitsi anu. Kodi mufuna kuti muwauze zomwe mukuchita kunyumba? Mungaikemo izi:
 - ⊕ Chomwe mwakondwera nacho kuchita
 - ⊕ Choseketsa chomwe chinachitika
 - ⊕ Chinthu chobvutako chomwe munachita
 - ⊕ Chinthu chomwe muchifunitsitsa kuti chichitike
- Lembani kalata muikepo keyala wa komwe mukhala ndi tsiku ndipo mulembe chisindikizo chanu munsi.
- Ngati nkotheka muipeleke nokha kalata kwa aphunzitsi anu. Mufunse wina wachikulire kapena m'bale wanu wamkulu akuthandizeni.

Dear Mrs Voter,

I thyed Tee nicks and I loved it. It was gummy when me and my Mum got tangled up in the sugar ball. I also thyed maths game, and all the different games on it. Some of them are difficult and some of them are really fun! I'm looking forward to making something out of next. yours

sincerely

This: 

Kuonjeza zochita:

- Kodi mungalembe kalata yoyerekeza kuti yachoka kwa aphunzitsi anu kuyankha kalata wanu? Gwiritsani nchito mau amene aphunzitsi anu anakalembo.
- Kodi mungalembe kalata yoseketsa kwa aphunzitsi anu kufutokoza chifukha chiyani simunalembe nchito akunyumba? Ganizirani kachifukwa kena-kena mwachitsanzo:
 - ⊖ “mbuzi inadya nchito yanga yakunyumba”
 - ⊖ “Chimphepo chinakuntha kwambiri ndipo chinatenga nchito yanga yakunyumba”
- Gwiritsani nchito ndondomeko yoyikika kuti ukuthandizeni kulemba kalata.

Kwa aphunzitsi

Chonde mundikhululukire chifukwa sindinachite nchito yakunyumba.

Mundichitire chifundo koma (chinachitika ndi chiyani?)

Ndidza (udzachita chiyani?)....

Mafuno abwino,

Ndine wanu:



Msinkhu: Aliyense

Kugwapo kwa akulu/abale: Mochepa

Zomwe mudzaphunzira: Kukhazikika kwachilankhulidwe, kulemba kalata, kupanga ziganizo, kupanga mau

Zomwe mudzachita: Kuchita zinthu mwaluso, kumvera momwe anvelera wina ndi mumuthandiza

Njira zina zochitiramo nchito:

- Werengani kalata wanu mokweza kwa munthu wina (mumuuze akulembereni)
- Mulembe kakalata kakang'ono
- Muwalembere chiyunzi-thunzi aphunzitsi anu chazinthu zomwe muli kuchita kunyumba